



## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

### NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

#### NYENGO MSABATAYI


#### KUYAMBIRA PA 21 MPAKA PA 27 OCTOBER, 2024

#### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Tiyembekezere nyengo ya **dzuwa ndi yotentha** kamba ka m'mpweya ofunda wochokera kumvuma. Koma pali kuthekera kwa mvula yamabingu m'madera ochepa am'chigawo cha kumpoto ndi okwera am'chigawo cha ku m'mwera.

#### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kuyambira masana a Lachiwiri pa 15 October mpaka Lachinayi pa 17 October, m'madera ambiri kunali kwa nyengo ya mphepo ndi yamitambo komanso kunagwa mvula yomwe inagwa ya mabingu ndi ya mphamvu m'madera ena. Mvula ya mphamvu inayezedwa pa 16 October ku Lisungwi EPA ya mulingo wa 99.5 mm, ku Phalula ya mulingo wa 81 mm, ndipo ku Chichiri ku Blantyre ya mulingo wa 52 mm. (Onani mapu m'munsimu).



Zithuzichi zikuonetsa ena mwa madera omwe analandira mvula pa 16 October ndi pa 17 October.

#### MALANGIZO MSABATALI

- **Nyengo yotentha ndi ya dzuwa:** Tizimwa madzi pafupipafupi komanso tisamakhalitse pa dzuwa.
- **Alimi:** Alimi akulimbikitsidwa kuti apeze **ulosi wa nyengo ya Dzinja la 2024/2025 wa madera awo** kuti athe kupanga zisankho zoyenera pa ulimi. (<https://www.metmalawi.gov.mw/products/seasonal-climate-outlook/the-2024-2025-seasonal-climate-outlook/>)

**Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:** The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: [metdept@metmalawi.gov.mw](mailto:metdept@metmalawi.gov.mw), Website:

[www.metmalawi.gov.mw](http://www.metmalawi.gov.mw)

**Malo osindikizira: Blantyre**

**Yatulutsidwa Lamulungu pa 20 October, 2024**